

CHIGONJETSO MWA YESU KHRISITU



Kolembedwa ndi Watson Goodman

Kaulere — Osagulitsa

CHIGONJETSO MWA YESU KHRISITU

Satana yemwe m'Bukhu Lopatulika limamunena kuti “mfumu ya dziko lapansi,” ndi mdani wamkulu wa Mulungu komanso munthu yemwe ndi wopambana pa zolengedwe zonse. Anthufe tiri pa malo ovuta kwambiri pomwe tikumenyana ndi Satana tisankhe pakati pa Ambuye awiriwa kuti adzatitsogolera mpaka muyaya ndi mdani KRISTU mlengiyemwe ndi Imanueli (Mulungu nafe) kapena Satana, wolengedwayemwe ndi mfumu youkila Mulungu. Kupyolera mu imfa ndi kuuka kwake, KRISTU anawagonjetsera onse omwe amamukhulupilira iye.

Satana amayesa kunyenga ndi kusocheretsa anthu. Chipembedzo ndi nkhani yaikuru. KRISTU, mlengi wathu, ayenera kupembedza. Tiyenera kufanana ndi iye yemwe tipembedza. Njira ya Satana zonyengera anthu ndizo: 1) kusadalira Mulungu, 2) kumvera ziwanda, 3) kupembedza “munthu wochimwa”, 4) kupembedza “chifanizo chake”, ndipo 5) chizindiro cha pathupi choyenereza kuti munthu agule ndi kugulitsa. Chenjerani ndi zimenezi!

—Watson Goodman (1920-2002)

MULUNGU SANALENGA MUNTHU WOTSUTSANA NAYE

1

Mulungu Analenga Lusifara kuti Akhale Kumwamba Pamalo Olemekezeka Kwambiri

“...Atero Ambuye Yehova, Wakomera muyeso ndi cizindikilo, wodzala ndi nzeru wokongola wangwiro. Unali m’Edene, munda wa Mulungu, mwala uli wonse wa mtengo wace unali copfunda cako, sardiyo, topazi, diamondi, berulo, sohamu, ndi yaspi, safiro, nofeki, bareketi, ndi golidi; malingaka ako ndi akazi ako anakutumikira tsiku lolengedwa iwe zinakonze keratu.”

Anali pafupi ndi mpando wachifumu wa Mulungu

“Unali kerubi wodzozedwa waku-

phimba, ndipo ndinakuika unali pa phiri lopatulika la Mulungu, anayendayenda pakati pa miyala yamoto.”

Analengedwa Wangwiro

“Unali wangwiro m’njira zako cilengedwere iwe, mpaka cinapezeka mwa iwe cosalungama.”

Mulungu Amatulutsa Tchimo

“Mwa... malonda ako anakudzaza m’kati mwako ndi ciwawa, ndipo unacimwa; cifukwa cace ndinakukankha kukucotsa pa phiri la Mulungu; ndipo ndinakuononga, kerubi wakuphimba iwe, kukucotsa pakati pa miyala yamoto.” —Ezekieli 28:12-16

CHINAYAMBITSA KUTI LUSIFARA ACHIMWE NDI CHIYANI?

Kunyada kutsogolera kuonongeka;
mtima wodzikuzwa ndi kutsogolera
kupunthwa. —Miyambo 16:18

“Unadzikuza mtima cifukwa ca
kukongola kwako, waipisa nzeru za-
ko; cifukwa ca kuwala kwako nda-
kugwetsa pansu, ndakuika pamaso
pa mafumu, kuti akupenye.”
—Ezekieli 28:17

Tsoka La Munthu Wogalukira

“Mwa mphulupulu zako zocuruka
ndi malonda ako osalungama wai-
psa malo ako opatulika; cifukwa ca-
ce ndaturutsa moto m’kati mwako

wakunyeketsa iwe; ndipo ndakusa-
ndutsa mapulusa panthaka pamaso
pa onse akuona. Onse akudziwa iwe
mwa mitundu ya anthu adzadabwa
nawe; wasanduka coopisa, ndipo su-
dzakhalanso konse.”

—Ezekieli 28:18, 19

Olengedwa Onse Amvere Namalenga

Tumikirani Yehova ndi cikondwe-
rero: Idzani pamaso pace ndi ku-
myimbira mokondwera. Dziwani
kuti Yehova ndiye Mulungu; Iyeyu
anatilenga, ndipo ife ndife ace; Ndi-
fe anthu ace ndi nkhusa za pabusa
pace. —Masalmo 100:2, 3

LUSIFARA ANADZINENERA YEKHA KUTI ANALI WODZIDALIRA YEKHA

3

“Wagwadi kucokera kumwamba, iwe nthanda, mwana wa mbanda kuca! Wagwetsedwa pansi, iwe wolefula amitundu! Ndipo iwe unati mumtima mwako, Ndidzakwera kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wacifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu; ndidzakhala pamwamba pa phiri la khamu, m'malekezero a kumpoto; ndidzakwera pamwamba pa mitambo, ndidzafanana ndi Wam'mwambamwamba.”

Wodzetsa Chionongeko pa Dziko Lapansi

“Koma udzatsitsidwa kungsi ku manda, ku malekezero a dzenje.

Iwo amene akuona iwe adzayang'anitsitsa iwe, nadzalingalira za iwe, ndi kuti, Kodi uyu ndi munthu amene ananthunthumiritsa dziko lapansi, amene anagwedeza maufumu; amene anapululutsa dziko, napasula midzi yace, amene sanamasula ndende zace, zinke kwao?”

“Mafumu onse a amitundu, onsewo agona m'ulemerero yense kunyumba kwace. Koma iwe watayidwa kunja kwa manda ako, ngati nthambi yonyansa, ngati cobvala ca ophedwa, opyozedwa ndi lupanga, otsikira ku miyala ya dzenje....”

—Yesaya 14:12-19

4 KUSATSAMIRA PA MULUNGU NDI KOOPSYA

Choyamba mwa Lusifara

Yesu anaŵauza kuti, “Ndinaona Satana alikugwa kuchokera Kumwamba ngati mphezi.”

—Luka 10:18

Mwa Angelo Otsatira Satana

... Mulungu sanalekerere angelo amene anachimwa aja, koma anaŵaponya m’ndende, m’maenje amdima momwe ali omangidwa kudikira chiweruzo.

—2 Petro 2:4

Satana Amalamulira Anthu

... Poti munthu amasanduka kapolo wa chimene chamugonjetsa.

—2 Petro 2:19

“Chifukwa kudzaoneka anthu onena monama kuti iwo ndi Mpulu-

mutsi wolonjezedwa uja, kapena kuti ndi aneneri. Azidzachita zizindikiro zodabwitsa ndiponso zinthu zozizwitsa, kuti ngati nkotheke asokeretse ngakhale anthu amene Mulungu anaŵasankha.” —Mateo 24:24

Kumwamba Kuyenera Kukhala Chifuniro Chimodzi Chokha —Chifuniro Changwiro cha Mulungu

Musamatsanzira makhalidwe oipa a dziko lino lapansi, koma Mulungu asinthe moyo wanu wonse pakukupatsani mitima yatsopano. Pamenepo mudzatha kudziŵa zimene Mulungu afuna, ndipo mudzazindikira zimene zili zabwino, zangwiro ndi zomkondweretsa. —Aroma 12:2

ZOMUYENERA MULUNGU PA CHIPEMBEDZO CHONSE

5

“Ine ndine Yehova Mulungu wako amene ndinakuturutsa m’dziko la Aigupto, m’nyumba ya akapolo. Usakhale nayo milungu yina koma Ine ndekha.” –Deuteronomo 5:6, 7

Mcitireni Yehova ulemerero wa dzina lace; bwerani naco copereka, ndipo fikani pamaso pace; lambirani Yehova m’ciyero cokometsetsa.
–1 Mbiri 16:29

“...Pembedzani Iye amene anale-nga thambo, dziko lapansi, nyanja, ndiponso akasupe a madzi.”
–Chibvumbulutso 14:7

Koma Yesu anati, “Choka, Sata-na! Malembo akuti, ‘Uzipembedza Ambuye Mulungu wako, ndipo uzi-tumikira Iye yekha.’” –Mateo 4:10

Tiyeni, tipembedze tiwerame; ti-gwade pamaso pa Yehova, amene anatilenga. (Onani Genesis 1:27.)
–Masalmo 95:6

Anthu Onyengedwa Amapembedza Woukira

...Anthu onse anatsata chilombo chija alikudabwa. Anapembedza chinjoka chija chifukwa chinapatsa u-lamuliro wake kwa chilombo chija. Anapambedzanso chilombo chija...
–Chibvumbulutso 13:3, 4

6 MUSAPEMBEDZE OTSUTSANA NDI MULUNGU

Satana Ndi Mizimu Yake Amalakalaka Chipembedzo

Potsiriza Satana anatenga Yesu napita naye paphiri lalitali kwambiri. Anamuonetsa maufumu onse a pansi pano ndi ulemerero wawo, namuuzza kuti, “Zonsezi ndidza-kupatsani mukagwada pansi ndi kundipembedza.” —Mateo 4:8, 9

Anthu ena onse otsala, amene sanaphedwe ndi miliri ija, sanalape ndi kusiya zimene anapanga ndi manja awo. Sanaleke kupembedza ziŵanda ndi mafano agolide, asiliva, amkuwa, ndi amtengo, amene sangathe kupenya, kapena kumva, kapena kuyenda.

—Chibvumbulutso 9:20

Mulungu Amaononga Anthu Opembedza Motere

...Ndipo zironda zonyansa ndi zopweteka zinabuka pa anthu onse aja, amene analandira chizindikiro cha chilombo chija, napembedza fano lake....Aliyense anaweruzidwa molingana ndi ntchito zake. Kenaka Imfa ija ndi Malo a anthu akufa aja zinaponyedwa m’nyanja yamoto. Nyanja yamoto imeneyi ndiyo imfa yachiŵiri.

—Chibvumbulutso 16:2; 20:13, 14

Ine ndine Yehova; dzina langa ndi lomweli; ndipo ulemerero wanga Ine sindidzapereka kwa wina, ngakhale kunditamanda kwa mafano o-
semedwa.

—Yesaya 42:8

***Angelo A Mulungu Ndi
Amphamvu Koposa Angelo
A Satana***

Lemekezani Yehova, inu angelo ace; a mphamvu zolimba, akucita mau ace, akumvera liu la mau ace.

—Masalmo 103:20

Ndipo kunabuka nkondo Kmwamba. Mikaele ndi angelo ake anachita nkondo ndi chinjoka chija. Chinjokacho pamodzi ndi angelo ake chinatengana nawo, koma sichi-
napambane....

—Chibvumbulutso 12:7, 8

Nanga angelo, si ndiwo mizimu yotumikira chabe, imene Mulungu

amaituma chifukwa cha iwo amene adzalandire chipulumutso?

—Aheberi 1:14

Pakuti adzalamulira angelo ace za iwe, akusunge m'njira zako zonse. Adzakunyamula pa manja ao, ungangunde phazi lako pamwala.

—Masalmo 91:11, 12

***Angelo A Satana (Mizimu Yoipa)
Ndi Olimba Mtima Kutengera
Anthu Kunyanja Yotentha Ndi Moto***

Mzimu Woyera alikunena momveka kuti pamasiku otsiriza anthu ena adzataya chikhulupiro chawo. Adzamvera anthu onyenga, nadzatsata ziphunzitso zochokera kuzi-
wanda.

—1 Timoteo 4:1

8 ANTHU KOMANSO ZINTHU ZIMENE SATANA AMADANA NAZO

Munthu, Wolengedwa M'chifuniro Cha Mulungu

Pamene mwanayo analikubwera, chiwandacho chinamgwetsa pansi ndi kumgwedeza kolimba. Koma Yesu anadzudzula chiwanda chonyansacho, ndipo atachiritsa mwanayo, anamperekanso kwa bambo wake.

—Luka 9:42

Kristu (Mulungu) Wokhala Ndi Chipulumutso mu Umunthu Wake Ndi Mwazi Wopatulika

Pamene Herode... anakwiya kwamбири. Anatuma anthu ku Betelehemu ndi kumalo ake onse ozungulira, kuti akaphe ana amuna onse a

zaka ziwiri ndi ocheperapo. Zaka zimenezi ndi monga iye anafunsitsira kwa akatswiri a nyenyezi aja.

—Mateo 2:16

Mau a Mulungu – Satana Amawatsutsa Mau A Mulungu

...“Ea! kodi anatitu Mulungu, ...?” Njokayo ndipo inati kwa mkaziyo, “Kufa simudzafai.”

—Genesis 3:1, 4

Okhulupilira Obadwa Ndi Mzimu

...Mdani wanu Satana amayendayenda ngati mkango wobangula namafunafuna woti amudye.

—1 Petro 5:8

***Satana Amatsanzira
Zizindikiro Monga Mwini***

Mumzindamo simudzapezekanso kanthu kalikonse kotembereredwa ndi Mulungu. Mpando wachifumu wa Mulungu ndi wa Mwanawankhosa uja udzakhala m'menemo, ndipo atumiki ake adzampembedza. Iwo adzaona nkhope yake, ndipo dzina lake lidzakhala lolembedwa pamphumi pawo.

—Chibvumbulutso 22:3, 4

(Onani kutsanzira kwa Satana, tsamba la 35.)

***Aipsya Uthenga Wabwino
Ndi Kunena Bodza***

Ndilikudabwa kuti mulikupatuka msangamsanga motere kusiya Mu-

lungu, amene anakuitanani mwa kukoma mtima kwake, ndipo kuti mulikutsata uthenga wabwino wina. Koma palibe konse uthenga wabwino wina. Pali anthu ena amene alikukusokonezani, ndipo alikufuna kupotoza Uthenga Wabwino wone-na za Kristu. —Galatia 1:6, 7

***Amatsanzira Aneneri A
Mulungu***

Anthu otereŵa sali atumwi oona, koma ndi antchito onyenga, amene amadzizimbaitsa, naoneka ngati atumwi a Kristu. Si zododometsa zimenezi ayi, pakuti Satana yemwe amadzizimbaitsa, naoneka ngati mngelo wounikira anthu.

—2 Akorinto 11:13, 14

Ana inu, dzisungeni bwino, osapembedza mafano. —1 Yohane 5:21

“Usakhale nayo milungu yina koma Ine ndekha. Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena cifanziro ciri conse ca zinthu za m’thambo la kumwamba, kapena za m’dziko lapansi, kapena za m’madzi a pansi pa dziko; usazipembedzere izo, usazitumikire izo....”

—Eksodo 20:3-5

***Milungu Yina Ndi Yonyansa
Pamaso Pa Mulungu. Nsembe
Ya Munthu Ndi Yoletsedwa***

“Muononge konse malo onse, amitundu amene mudzawalanda anatumikirako milungu yao, pa mapiri

atali, ndi pa zitunda, ndi pansi pa mitengo yonse yabiriwiri. Dzicenjerani nokha mungakodwe ndi kuwatsata, ataonongeka pamaso panu.... Musamatero ndi Yehova Mulungu wanu; pakuti ziri zonse zinyansira Yehova, zimene azida Iye, iwowa anazicitira milungu yao; pakuti angakhale ana ao amuna ndi ana ao akazi awatentha m’moto, nsembe ya milungu yao.”

—Deuteronomo 12:2, 30, 31

...Kodi ndipereke...cipatso ca thupi langa cifukwa ca kucimwa kwa moyo wanga? —Mika 6:7

Mwazi wa Yesu Kristu umachotsa machimo athu.

Anasiya zoonza za Mulungu natsata zabodza. Anapembedza natumikira zolengedwa, m'malo mwa kupebedza ndi kutumikira Mlengi mwini, amene tiyenera kumlemekeza mpaka muyaya. Amen.

—Aroma 1:25

Koma Mulungu wathu ndiye ali m'mwamba; acita ciri conse cimkonda. Mafano ao ndiwo a siliva ndi golidi, nchito za manja a anthu. Pakamwa ali napo, koma osalankhula; maso ali nao, koma osapenya; makutu ali nao, koma osamva; mphuno ali nazo, koma osanunkhiza; manja ali nao, koma osagwira; mapazi ali nao, koma osayenda; kapena sarena pammero pao. Adzafanana nao

iwo akuwapanga; ndi onse akuwakhulupirira. —Masalmo 115:3-8

***Kupembedza Mafano Ndiko
Kupembedza Mizimu Yoipa,
Kapena Satana***

...Peŵani kupembedza mafano. Iyayi koma kuti zimene anthu akunja amapereka nsembe, amapereka kwa ziŵanda, osati kwa Mulungu...

—1 Akorinto 10:14, 20

***Chilango Chobwera
Chifukwa Chopembedza Mafano***

“...Opembedza mafano,...malo awo ndi m'nyanja yamoto woyaka ndi miyala ya sulufure. Imeneyi ndiyo imfa yachiŵiri.”

—Chibvumbulutso 21:8

12 MULUNGU AMADANA NDI KUPEMBEDZA MAFANO

*Mulungu Anaononga Mitundu
Cifukwa Cha Mafano
Awo – Musasunge
Mafano M'nyumba Mwanu.*

“...Palibe munthu mmodzi adzaima pamaso panu, kufikira mutawaononga. Mafano osema a milungu yao muwatenthe ndi moto; musamasirira siliva ndi golidi ziri pa iwo, kapena kudzitengera izi; mungakodwe nazo; pakuti izi zinyansira Yehova Mulungu wanu. Musamalowa naco conyansaci m'nyumba mwanu, kuti mungaonongeke konse pamodzi naco....”

—Deuteronomo 7:24-26

*Cifukwa ninji panali A'Israyeli ambiri
amene anagwidwa ndi mizimu yoi-*

pa pamene Kristu analalikira padziko lapansi? Cifukwa akholo awo anapembedza mizimu yoipa!

Ndipo anatumikira mafano ao, Amene anawakhalira msampha: Ndipo anapereka ana ao amuna ndi akazi nsembe ya kwa ziwanda, potero udayaka mkwiyo wa Yehova pa anthu ace, Nanyansidwa Iye ndi colowa cace. —Masalmo 106:36, 37, 40

Usazipembedzere izo, usazitumiki-re izo; cifukwa Ine Yehova Mulungu wako ndiri Mulungu wansanje, wakulanga ana cifukwa ca atate ao, kufikira mbadwo wacitatu ndi wacinai wa iwo amene akudana ndi Ine.

—Eksodo 20:5

“Wanyanga usamlola akhale ndi moyo.”
—Eksodo 22:18

“Musamatembenukira kwa obwebweta, kapena anyanga; musawafuna, ndi kudetsedwa nao....”
—Levitiko 19:31

Ndipo ndidzaononga zanyanga za m’dzanja lako; ndipo sudzakhalanso nao alosi.
—Mika 5:12

“Pakuti kupanduka kuli ngati coipa ca kucita nyanga, ndi mtima waliuma uli ngati kupembedza milungu yacabe ndi maula. Popeza inu munakaniza mau a Yehova, Iyenso anakaniza inu, kuti simudzakhalanso mfumu.”
—1 Samueli 15:23

“Mutakalowa m’dziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani,

musamaphunzira kucita monga mwa zonyansa za amitundu aja. Asapezeke mwa inu munthu wakupitiriza mwana wace wamwamuna kapena mwana wace wamkazi ku moto wa ula, wosamalira mitambo, kapena wosamalira kulira kwa mbalame, kapena wanyanga. Kapena wotsirika, kapena wobwebweta, kapena wopenduza, kapena wofunsira akufa. Popeza ali yense wakucita izi Yehova anyansidwa naye; ndipo cifukwa ca zonyansa izi Yehova Mulungu wanu awapitikitsa pamaso panu.”
—Deuteronomo 18:9-12

Matsenga: Kunena za mtsogolo pombenza maula ndi kukhulupilira mizimu ya anthu akufa.

14 KUNENA ZA MTSOGOLO POTHANDIZIDWA NDI MIZIMU YOIPA

***Mulungu Amaletsa Nyanga,
Kuombeza Maula ndi
Kudzitema Mphini***

“Musamadya kanthu ndi mwazi wace; musamacita nyanga, kapena kuombeza ula. Musamadziceka matupi anu cifukwa ca akufa, kapena kutema mphini; Ine ndine Yehova.”
—Levitiko 19:26, 28

“Koma inu, musamvere aneneri anu, kapena akuombeza anu, kapena maloto anu, kapena alauli anu, kapena obwebweta anu....”
—Yeremiya 27:9

“...Ndipo ndidzakhala mboni yakufulumira kutsutsa obwebweta,

ndi acigololo, ndi olumbira monama....”
—Malaki 3:5

Pakuti aterafi anena zopanda pace, ndi aula aona bodza; nafotokoza maloto acabe, asangalatsa nazo zopanda pace; cifukwa cace ayendayenda ngati nkhosa, azunzika popeza palibe mbusa. —Zekariya 10:2

Khulupirirani Mbasa Weniweni
[Yesu anati,] “Mtima wanu usabvutike. Khulupirirani Mulungu, khulupirirani Inenso.” —Yohane 14:1

Matsenga: Kuneneratu za mtsogolo zomwe ndi zosadziwika pogwiritsa ntchito njira zonama.

Tsenga: Mizimu yoipa ichita tsenga.

***Kucita Matsenga Ndi Mizimu
Yodziwika Bwino***

Ndipo pamene iwo adzati kwa iwe, “Funa kwa olaula, ndi obwebweta, amene alira pyepye, nang’ung’udza,” kodi anthu sadzafuna kwa Mulungu wao?... –Yesaya 8:19

***Kugwiritsa Ntchito Ziwalo
Zina za Thupi***

“Pakuti mfumu ya ku Babulo aima pa mphambano ya njira, polekana njira ziwirizo, kuti aombeze maula; agwedeza mibvi, afunsira kwa aterafi, apenda ndi ciwindi.”
–Ezekieli 21:21

***Kucita Matsenga Pogwiritsa
Ntchito Ndodo***

Anthu anga afunsira ku mtengo

wao, ndi ndodo yao iwafotokozerana; pakuti mzimu wacigololo wawalankwitsa, ndipo acita cigololo kuukera Mulungu wao. –Hoseya 4:12

***Kulangidwa Chifukwa
Chochita Matsenga***

Momwemo Sauli anafa, cifukwa ca kulakwa kwace analakwira Yehova, kulakwira mau a Yehova amene sanawasunga; ndiponso cifukwa ca kufunsira wobwebweta, kufunsirako, osafunsira kwa Yehova....
–1 Mbiri 10:13, 14

“Ndipo alauli adzacita manyazi, ndi olosa adzathedwa nzeru;... pakuti kuyankha kwa Mulungu kulibe.”
–Mika 3:7

M'MENE A KARONGA A DZIKO LAPANSI AMACHITIRA

Anthu Akunja Amatsata Zizindikiro Za M'thambo Kapena Nyenyezi

Atero Yehova, “Musaphunzire njira ya amitundu, musaope zizindikiro za m'thambo; pakuti amitundu aziopa izo.”
—Yeremiya 10:2

Musamakhulupilire malemba kapena zinthu zina kuti mukhale ndi mwayi kape-nanso kugonjera nyimbo ndi zithunzi zo-ipa. “**Sindidzaika cinthu coipa pamaso panga...**” (Masalmo 101:3.) Siyani kunyada, chinyengo, ndipo chipembedzo choipa.

“Muli ndi tsoka, ... inu anthu achi-phamaso! ... amene amaoneka oko-ngola kunja, koma chonsecho,

m'kati mwake ngodzaza ndi... zonyansa zina zonse.” —Mateo 23:27

Kudzipha Kumachokera Kwa Satana

Musakhulupilire bodza la Satana, kapena mizimu yoipa loti akuuzeni ngati kudzipha nokha mudzasiyana ndi mavuto ndikukhala opanda chikumbumtima! “**Usaphe**” (Eksodo 20:13.)

Ndi Kristu Yekha Amatimasula Kuchokera Ku Machimo

(Onani Masamba 48 ndi 49.)

Yehova ndiye mphamvu yanga ndi nyimbo yanga, Ndipo wakhala cipulumutso canga....

—Eksodo 15:2

Kupyolera Mwa Aneneri Onyenga

Ndipo Yehova anati kwa ine, “Aneneri anenera zonama m’dzina langa; sindinatuma iwo, sindinauza iwo, sindinanena nao; anenera kwa inu masomphenya onama, ndi ula, ndi cinthu cacabe, ndi cinyengo camtima wao.” —Yeremiya 14:14

Kupyolera Mkulankhula Ndi Anthu Akufa

Motsogozedwa ndi Mulungu, Mfumu Davide ananena za mwana wake wamwamuna, “Koma tsopano wafa, . . . iye sadzabweranso kwa ine.”

—2 Samueli 12:23

Osalankhulana ndi mizimu yoipa, koma kuilamula mizimuyo m’dzina

la Kristu kuti ichoke. Osakhulupilira kuombeza maula kapena kuombezera ulendo ndi ufiti uliwonse. “... Wopulumutsa ndiye Yehova” (Miyambo 21:31.)

Tayani Mafano, Kapena Mabuku Onena Za Usatana

Ambiri amene analikuchita matsenga, anasonkhanitsa mabuku awo naŵatentha pamaso pa anthu onse. Pamene anaonkhetsa mtengo wake wa mabukuwo, anapeza kuti unakwanira ngati makwacha masauzande asanu. Motero mawu a Mulungu ananka nafalikirafalikira ndi kugwira ntchito mwamphamvu.

—Ntchito 19:19, 20

(*Werengani Genesis 35:2-5.*)

KRISTU ANALENGA UKWATI – SATANA ALEKANITSA UKWATI

Ndipo nthitiyo anaicotsa Yehova Mulungu mwa Adamu anaipanga mkazi, ndipo ananka naye kwa Adamu. Cifukwa coteru mwamuna adzasiya atate wace ndi amace nazadziphatika kwa mkazi wace: ndipo adzakhala thupi limodzi.

–Genesis 2:22, 24

Ukwati muziulemekeza nonse, ndipo amuna ndi akazi awo azikhala okhulupirika, pakuti adama ndi achigololo Mulungu adzaŵalanga.

–Aheberi 13:4

Lamulo langa (osatinso langa, koma la Ambuye) kwa anthu a m'banja ndi ili: Mkazi asalekane ndi mwamuna wake. Koma ngati amle-

ka, akhale wosakwatiŵanso, kapena ayanjanenso ndi mwamuna wakeyo. Chimodzimodzinso mwamuna asasudzule mkazi wake.

–1 Akorinto 7:10, 11

(Onani Aroma 7:2; Marko 10:9.)

Munthu amene amachimwa, ngwa Satana, pakuti Satana ngochimwa kuyambira pachiyambi...

–1 Yohane 3:8

Inu Mumakhala Munthu Wa Yemwe Mukumumvera

Mudziŵa kuti mukadzipereka kukhala akapolo a munthu wina ndi kumamumvera, pamenepo ndinu akapolo a munthuyo amene mumamumvera...

–Aroma 6:16

KUCHITA CIGOLOLO NDI CHIWEREWERE NDI KUGALUKIRA MULUNGU

19

“Usacite cigololo.” –Eksodo 20:14

Chimene Mulungu afuna ndi chakuti mukhale oyera mtima, ndiye kuti muzipeŵa dama.

–1 Atesalonika 4:3

“Munthu akacita cigololo ndi mkazi wa mwini, popeza wacita cigololo ndi mkazi wa mnansi wace, awaphe ndithu, mwamuna ndi mkazi onse awiri.”

–Levitiko 20:10

Ndi izi: dama, kuchita zonyansa, kusadziletsa, ...kuti iwo amene amachita zotere, sadzalandirako Ufumu wa Mulungu. –Agalatia 5:19, 21

Kuchimwira Thupi Lanu

... Thupi la munthu si lochitira da-

ma, koma nla Ambuye, ndipo Ambuye ndiwo eni ake thupilo. Kodi simudziŵa kuti matupi anu ndi ziŵalo za Kristu?... Thaŵani dama. Tchimo lina lililonse limene munthu achita siliipitsa thupi lake, koma munthu wadama amachimwira thupi lake lomwe.

–1 Akorinto 6:13, 15, 18

Anakubala Athandize Ana Awo Kuti Anawo Asacite Cigololo

Usamaipsa mwana wako wamkazi ndi kumcititsa cigololo; lingadzale ndi cigololo dzikoli, ndi kudzazidwa nazo zocititsa manyazi.

–Levitiko 19:29

Monga anthu onse amamwalira chifukwa ndi ana a Adamu, momwemonso anthu onse adzauka chifukwa ali mwa Kristu.

—1 Akorinto 15:22

Tsono popeza kuti anawo ndi anthu, okhala ndi magari ndi mnofu, Yesu yemwe anasanduka munthu wonga iwowo. Iye anachita zimenezi kuti ndi imfa yake awononge Satana, amene anali nayo mphamvu paimfa. Anachitanso zimenezi kuti amasule iwo amene pamoyo wawo wonse anali ngati akapolo chifukwa choopa imfa.

—Aheberi 2:14, 15

...Mwana wa Mulungu anaoneka ndi cholinga chakuti awononge zo-

chita za Satana. —1 Yohane 3:8

Tikakhala Mwa Kristu Mzimu Wathu Sudzafa

Iye anatipulumutsa, ndipo anatitana kuti tikhale anthu ake. Sanachite zimenezi chifukwa kuti ife tinachita zabwino ayi, koma chifukwa Iye mwini anazikonzeratu motere, ndiponso chifukwa mwa Kristu Yesu anatikomera mtima nthawi isanayambe. Koma tsopano, Mulungu watiululira zimenezi mwa kubwera kwa Mpulumutsi wathu, Kristu Yesu. Kristuyo anathetsa mphamvu ya imfa, ndipo mwa Uthenga Wabwino anaonetsera poyera moyo umene sungafe konse.

—2 Timoteo 1:9, 10

...Mdani wanu Satana amayenda-yenda ngati mkango wobangula namafunafuna woti amudye. Limbanani naye mutakhazikika m'chikhulupiriro....

—1 Petro 5:8, 9

Bvalani zida zonse zimene Mulungu akupatsani, kuti muthe kulimbika pakukana machenjerero a Satana... mutabvala choona ngati lamba m'chiuno mwanu. Bvalani chilungamo ngati malaya achitsulo otchinjirizira pachifuwa chanu, ndipo kukonzeka kwanu kulalika Uthenga Wabwino wa mtendere kukhale ngati nsapato zanu. Nthaŵi zonse mukhale ndi chikhulupiriro ngati chisyaŵo chanu, chimene mudzatha kuzi-

mitsira mibvi yonse yoyaka moto ya Satana. Landirani chipulumutso ngati chisoti chanu, ndi mawu a Mulungu ngati lupanga limene Mzimu Woyera akupatsani... Panthaŵi iliyonse pempherani... ndi Mzimu Woyera.

—Aefeso 6:11-18

Mugonjere Mulungu tsono. Mukane Satana, ndipo adzakuthaŵani.

—Yakobo 4:7

...[Kristu] amene ali mwa inu, ngopambana Satana amene ali mwa anthu ongokonda zapansi pano.

—1 Yohane 4:4

Chifukwa chiyani Satana amathawa? Cifukwa Kristu ali mkati mwanu!

Iye Ndiye Mau A Mulungu

... Mulungu... koma pamasiku o-
tsiriza ano walankhula nafe kudzera
mwa Mwana wake. Ndi Iyeyu Mu-
lungu analenga zolengedwa zonse,
ndipo anamuika kuti akhale mwini
zonse.

—Aheberi 1:1, 2

Anthu anadabwa ndi kaphunzitsi-
dwe kake, chifukwa pophunzitsa a-
nalikusiyana ndi aphunzitsi a Ma-
lamulo a Mose, popeza kuti Iye a-
nkaphunzitsa ndi ulamuliro.

—Marko 1:22

Chifukwa analikuwaphunzitsa mo-
nga mwini mphamvu, osati monga
m'mene aphunzitsi a Malamulo a-
nkachitira.

—Mateo 7:29

“Ndipo anapatsa Mwanayo mpha-
mvu yoweruzira milandu, chifukwa
ndiye Mwana wa Munthu.”

—Yohane 5:27

Yesu anapita Kumwamba, ndipo
ali kudzanja lamanja la Mulungu.
Kumeneko angelo ndi maulamuliro
ndi zimphamvu zimamvera Iye.

—1 Petro 3:22

Pakuti Kristu anamwalira nakhala-
nso ndi moyo, kuti akhale Mbuye
wa anthu akufa ndiponso wa anthu
amoyo.

—Roma 14:9

Yesu anadza pafupi naŵauza kuti,
“Mphamvu zonse zapatsidwa kwa
Ine Kumwamba ndiponso pansi pa-
no.”

—Mateo 28:18

Yesu anadzuka, ndipo analetsa mphepoyo, nalamula nyanja kuti, “Tonthola! Khala bata!” Mphepo ija inalekadi, ndipo kunagwa bata lalikulu.
—Marko 4:39

***Iye Anachiza Ndi
Ulamuliro Wake***

“Ndikuonetsani kuti Mwana wa Munthu ali ndi mphamvu zokhulukira machimo panso pano.” Apo anauza munthu wa ziŵalo zakufa uja kuti, “Ndilikukulamula, dzuka, tenga tchika lako, uzipita kwanu.” Munthu uja anadzukadi, natenga tchika lija ndi kutuluka, onse aja akuona. Onsewo anazizwa kwambiri, natamanda Mulungu....

—Marko 2:10-12

Apo chiŵanda chinkamui pitsa chija chinamgwedeza kwamphamvu, ndipo chinakuŵa kwambiri, ndi kutuluka mwa iye. Anthu onse anadabwa kwambiri, mpaka kumafunsana kuti, “Kodi zimenezi nzotani? Zimenezitu ndi ziphunzitsa zatsopano. Ngakhale ziŵanda zonyansa zomwe akuzilamula ndi mphamvu, ndipo zikumumveradi.” —Marko 1:26, 27

Tsono anafika pafupi nakhudza chithatha. Anthu amene analikunyamula malirowo anaima, ndipo Yesu anati, “Mnyamata iwe, ndikukuuza kuti, Uka.” Pamenepo wakufayo anakhala tsonga nayamba kulankhula, ndipo Yesu anampereka kwa mayi wake.
—Luka 7:14, 15

24 KRISTU AMAPATSA OTSATIRA AKE MPHAMVU NDI ULAMULIRO OPAMBANA MPHAMVU YA MDANI

“Ndilikukupatsani mphamvu kuti muziponda njoka ndi zinkhanira, ndiponso kuti muzipambana mphamvu zonse za mdaniyo. Palibe kanthu kamene kangakupwetekeni.”

—Luka 10:19

Yesu anaitana ophunzira ake khumi ndi awiri aja nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro paziwanda zonse, ndiponso zochiritsira nthenda.

—Luka 9:1

...“Zoonadi, ngati mukhulupirira Mulungu, mungathe kulamula phiri ili kuti, ‘Nyamuka, kadziponye m’nyanja!’ Mutanenadi ndi mtima wosapeneka, koma ndi chikhulupiri-

ro kuti chimene mukunenacho chichitikadi, chidzachitikadi.”

—Marko 11:22, 23

Yesu anati, “Bwanji mukuti, ‘Ngati mungathe’? Zinthu zonse nzotheka kwa yemwe ali ndi chikhulupiriro.”

—Marko 9:23

Ndiponso mudziwe mphamvu yake yaikulukulu imene ilikugwira ntchito mwa ife omkhulupirira. Mphamvuyi ndi yomwe ija yolimba koposa.

—Aefeso 1:19

Ndingathe kuchita zonse chifukwa Kristu amandipatsa mphamvu.

—Afilipi 4:13

***Idzudzuleni. Ilamuleni Kuti
Ituluke M'dzina La Yesu***

Chiwândacho chinanena mawu ameneŵa chifukwa Yesu nkuti atachilamula kuti, “Chiwânda chonyansawe, tuluka mwa munthuyu!” Yesu anamfunsa munthuyo kuti, “Dzina lako ndani?” Iye nayankha kuti, “Dzina langa ndine ‘Chikhamu’, chifukwa tilipo ambiri.” ...Tsono ziwânda zonyansazo zinatuluka mwa munthu uja, ndipo zinakaloŵa m'nkumbazo.... –Marko 5:8, 9, 13

... Yesu... analamula chiwânda chonyansacho kuti. “Iwe chiwânda choletsa kulankhula ndi kumva, ndikukulamula kuti utuluke mwa mwa-

nayu, ndipo usadzaloŵenso mwa iye.” Chiwândacho chinapfuula ndipo chinamzunguza mwaphamvu mwana uja, kenaka nkutuluka. Mwanayo anangokhala ngati kuti wafa, mpaka ambiri nkumati, “Watsirizika!” Koma Yesu anamgwira dzanja namdzutsa, ndipo mwanayo anaimirira. ... “Chiwânda cha mtundu umenewu, mapemphero okha ndiwo angachitulutse.”

–Marko 9:25-27, 29

... Paulo... anapotoloka nauza chiwânda chija kuti, “Ndilikukulamula m'dzina la Yesu Kristu kuti utuluke mwa iye.” Ndipo chinatulukadi nthawi yomweyo. –Ntchito 16:18

Chifukwa cha chimenechi Mulu-ngu anamkweza kopambana, nam-patsa dzina lopambana dzina lina lililonse. Anachita zimenezi kuti zinthu zonse za Kumwamba, za pa-nsi pano, ndiponso za pansi padzi-

ko, zidzagwade pansi ndi kuchitira ulemu dzina la Yesu. –Afilipi 2:9, 10

“Chilichonse chomwe mudzachi-pemphe m’dzina langa ndidzachita, kuti Atate akalemekezedwe chifu-kwa cha Mwana.” –Yohane 14:13

Banja langa ndi ine, tinapita ku Africa kukagwira ntchito ya Kristu. Ndi-nadzuka usiku wina nditamva mzimu woipa uli pamwamba panga. Ndina-vutika, naopa kwambiri, koma ndinalira, “Yesu, ndithandizeni!” Panthawi yomweyo mzimuwo unacoka kusabweranso. M’dzina la Yesu Kristu muli-ndi mphamvu yodabwitsa kupambana Satana ndi mizimu yoipa yonse. Ita-nani pa dzina la Yesu Kristu kukupulumutsani inu (Aroma 10:13).

Mkazi wina anandiuza ine ndi mkazi wanga kuti pamene iye anali mtsika-na, napita kusukulu, mwamuna wina anamvutitsa nayesa kumupha. Mkazi-

yo anapfuula m'dzina la Yesu Kristu. Nthawi yomweyo mwamunayo sanakhoza kuchita kanthu kali konse, naleka kumvutitsa. Ndipo sanayesanso kuvutitsa mtsikanayo.

Mkazi wina anandiuza ine ndi mkazi wanga kuti pamene anali wamng'ono analoleza gulu la anthu a maula kuti alowe m'nyumba mwake. Atatero mizimu yoipayo inayamba kusuntha mipando ndi matebulo m'nyumbamo. Atavutika choncho, anatulutsa anthuwo m'dzina la Yesu, nadzipoleka kwathunthu kwa Yesu Kristu.

Musamumvere chisoni Satana kapena mizimu yoipa. Cholinga chake ndi chakuti inu mukhale mbali yake osati ya Mulungu. Mkristu wachikulire yemwe anali wofoka ndi wosokonezeka m'maganizo anandiuza zomwe Santana ankamuuzza. Ndinanena kuti Satana ndi mbuye wabodza ndipo sitiye-nera kumumvera. Ndinamudzudzula mudzina la Yesu. Munthuyo anati, "Ndakondwera kuti munabwera usiku uno". Anaoneka kuti anali ndi mte-ndere sabata zisanu asanamwalire.

—Watson Goodman

Kristu Ndiye Mulungu Mlengi

Mwa Iye Mulungu analenga zonse za kuthambo ndiponso za pansi pano, zooneka ndiponso zosaoneka, mafumu, akuluakulu, aulamuliro ndiponso amphamvu. Mulungu analenga zonse mwa Iye, ndipo zonse zimalinga kwa Iye. —Akolose 1:16

Kristu Amapatsa Kuwala Ndi Mtendere

“Kuwalako kudzaunikira onse okhala mumdima ndi mumthunzi wa imfa, ndipo kudzatitsogolera panjira yamtendere.” —Luka 1:79

Ambuye mwini, amene amapatsa mtendere, akupatseni mtendere nthawi zonse.... —2 Atesalonika 3:16

Mizimu Yoipa Ndi Satana Amaononga

“Wakuba amangodzera kuba, kupa ndi kuwononga...”

—Yohane 10:10

“...Koma muli ndi tsoka, dziko lapansi...pakuti Satana watsikira kwa inu. Ali wokalipa kwamбири....” —Chibvumbulutso 12:12

Satana Amapatsa Mdima Ndi Masautso

Njira ya oipa ikunga mdima....

—Miyambo 4:19

“...Munthu wachuma uja nayenso anamwalira, naikidwa m’manda. Pamene analikuzunzika ku Malo anthu akufa, anayang’ana kumwamba....” —Luka 16:22, 23

Kristu Ndiye Choonadi

Mawuwo anasanduka munthu, nazakhala pakati pathu. Tinaona ulemerero wake umene Iye, Mwana mmodzi yekha wa Atate, anaulandira kwa Atate ake. Anali wokoma mtima ndi wona kotheratu.... “Ngati musunga mawu anga nthawi zonse.... Mudzadziwa choona, ndipo choonacho chidzakupatsani ufulu.”

—Yohane 1:14; 8:31, 32

***Kristu Ndi Wodzala
Ndi Chikondi***

Tazindikira chikondi tsopano pa kuona kuti Kristu anapereka moyo wake chifukwa cha ife. Choncho ifenso tiyenera kupereka moyo wa-

thu chifukwa cha anzathu.

—1 Yohane 3:16

Satana Ndiye tate Wabodza

“Inu ndinu ana a Satana. Iye ndiye tate wanu, ndipo mulikufuna kumachita zimene tate wanuyo amalikalaka. Iyeyu kuyambira pachiyambi ndithu amapha anthu. Sali pazoonu, chifukwa mwa iye mulibezoonu. Kunena bodza ndilo khali-dwe lake, pakuti iye ngwabodza, ndiyenso tate wa mabodza onse.”

—Yohane 8:44

Satana Amabweretsa Chidani

“Ngati anthu ongokonda zapansipano adana nanu, kumbukirani kuti anadana ndi Ine asanadane nanu.”

—Yohane 15:18

Kristu Amasambitsa Mtima

Koma tikamayenda m'kuwala, ... pamenepo tilikuyanjana tonsefe. Ndipo magazi a Yesu, Mwana wake, amatisambitsa ndi kutichotsera tchimo lililonse. —1 Yohane 1:7

Kristu Amapulumutsa***Kuchokera Ku Machimo***

... Makamaka adzatipulumutsanso ndithu kumkwiyo wa Mulungu. —Aroma 5:9

***Kristu Amapatsa Moyo
Wosatha***

“Ndipo moyo wosathawo ndi wakuti akudziweni Inu, amene nokhanu ndinu Mulungu weniweni, ndipo adziwenso Yesu Kristu amene munamtuma.” —Yohane 17:3

Satana Amaipitsa Mtima

Musadzinyenge, nkosatheka kupusitsa Mulungu. Zimene munthu amabzala, adzakolola zomwezo, Chimene munthu amene angodzikhulupirira yekha adzakolole, ndi imfa. ... —Agalatia 6:7, 8

***Satana Amanyengelera Anthu
Kuti Achimwe***

Munthu amene amachimwa, ngwa Satana. ... —1 Yohane 3:8

***Satana Amatsogolera Anthu
Ku Imfa Yosatha***

“... Namsongole uja ndiwo anthu a Woipa uja. ... anazulira namsongole uja ndi kumtenta pamoto. ...” —Mateo 13:38-40

SATANA NDI ULAMULIRO WA DZIKO LONSE LAPANSI

31

Satana Ndiye Mfumu Ya Dziko Lapansi

“Sindilankhula nanunso zambiri tsopano ayi, pakuti Satana, mfumu ya anthu oipa a dziko lapansi, alikudza. Iyeyo alibe ulamuliro pa Ine.”
—Yohane 14:30

Ngati zina sizikuyenda Bwino, Mumuzenge Iye Mulandu

Nzeru zotere si zochokera Kummwamba, koma nza pansi pano, za anthu chabe, ndiponso nzochochera kuziŵanda. Pakuti pamene pali kaduka ndi kudzikonda, pomweponso pali chisokonezo ndi ntchito yoipa ya mtundu uliwonse.

—Yakobo 3:15, 16

Khalani Okhulupirika Kwa Kristu Kufikira Imfa

Anthu aja alikumponya miyala Stefano, Stefanoyo anapemphera kuti, “Ambuye Yesu, landirani mzimu wanga.” Ndipo anagwada pansi napfuula kolimba kuti, “Ambuye, musaŵaŵerengere tchimo ili.” Atanena mawu ameneŵa, anamwalira.
—Ntchito 7:59, 60

Za kuenjezera ulamuliro wace, ndi za mtendere sizidzatha pa mpando wacifumu wa Davide, ndi pa ufumu wace, kuukhazikitsa, ndi kuucirikiza ndi ciweruziro ndi cilungamo kuyambira tsopano ndi kunkabe nthawi zonse....
—Yesaya 9:7

WOKANA KRISTU – MFUMU YA DZIKO IDZABWERA

Abale, kunena za kubweranso kwa Ambuyathu Yesu Kristu, ndiponso za kusonkhana kwathu pamodzi kwa Iye... Musalole kuti munthu aliyense akupusitseni mwa njira iliyonse. Pakuti lisanafike tsikulo, kudzayamba kwachitika Chipatuko chachikulu, ndiponso kudzaoneka Munthu Woipitsitsa uja, amene aye-nera kutayika. Ndiye mdani, ndipo adzadziika pamwamba pa chilichonse chimene anthu amachitcha mulungu kapena amachipembedza, koterokuti adzadzikhazika m'Nyumba ya Mulungu ndi kudzitcha Mulungu. Ndipo pambuyo pake Munthu Woipitsitsa uja adzaululuka. Ambu-

ye Yesu adzamupha ndi mpweya wotuluka m'kamwa mwake, nadzamuwononga ndi maonekedwe ake aulemerero pamene adzabwere. Munthu Woipitsitsa uja adzabwera ndi mphamvu za Satana. Adzachita zamphamvu zosiyanasiyana, ndiponso zizindikiro ndi zozizwitsa zonyenga.

—2 Atesalonika 2:1, 3, 4, 8, 9

...Chinjoka chija chinapatsa chilombocho mphamvu yake, mpando wake wachifumu, ndiponso ulamuliro waukulu... Chinapatsidwanso mphamvu yolamulira pfuko lililonse, anthu a mtundu uliwonse, ndiponso a chinenero chilichonse.

—Chibvumbulutso 13:2, 7

WOKANA KRISTU ADZACHITA NKHONDO NDI OYERA MTIMA

33

Nidzanena mau akutsutsana ndi Wam'mwambamwamba, nidzaleme-tsa opatulika a Wam'mwambamwamba, nidzayesa kusintha nthawizo ndi cilamulo; ndipo adzaperekedwa m'dzanja lace mpaka nthawi imodzi, ndi nthawi zina, ndi nthawi yanusu. —Danieli 7:25

... Chinapatsidwanso mphamvu yolamulira miyezi 42. Tsono chinayamba kunena mawu onyoza Mulungu, dzina lake, malo ake okhalamo, ndiponso onse okhala Kumwamba. Chinaloledwa kuchita nkondo ndi anthu a Mulungu ndi kuwagonjetsa. Chinapatsidwanso mphamvu yolamulira pfuko lililonse, a-

nthu a mtundu uliwonse, ndiponso a chinenero chilichonse. Anthu onse okhala padziko lapansi adzachipe-mbedza. Ndiye kuti aliyense amene, chilengedwere dziko lapansi, dzina lake silinalembedwe m'buku la amoyo la Mwanawankhosa amene anaphedwa. Ngati wina ali ndi makutu, amve.

—Chibvumbulutso 13:5-9

Uzimenya nkondo yabwino ya kusunga chikhulupiriro, mpaka ukalandire moyo wosatha. Pakuti Mulungu anakuitanira zimenezi, ndipo unabvomera bwino chikhulupiriro chako pamaso pa mboni zambiri.

—1 Timoteo 6:12

OSAPEMBEDZA CHIFANIZO CHA OKANA KRISTU

***Mtsogoleri wa mpingo pa
dziko lonse lapansi
amathandiza Okana Kristu
kuti anyenge dziko lapansi.***

Chinalikunyenganso anthu okhala padziko lapansi ndi zozizwitsa zimene chinaloledwa kuchita pamaso pa chilombo choyamba chija. Chinauza anthu okhala padziko lapansi kuti apange fano lolemekezera nalo chilombo chija chimene chinalasidwa ndi lupanga, komabe chinakhala ndi moyo. Chinaloledwa kuuzira mpweya wopatsa moyo mufano lija la chilombo choyamba chija, kuti mpaka lilankhule, ndi kuphetsa ali-yense wosalipembedza. Chilombo-

cho chinagwidwa pamodzi ndi mneneri wonama uja amene anali atachita zozizwitsa pamaso pake.... Ndiponso anthu amene anali atapembedza fano lake lija. Chilombo chija ndi mneneri wonama uja, onse aŵiri anaŵaponyera m'nyanja yamoto....

—Chibvumbulutso 13:14, 15; 19:20

***Anthu A Mulungu Amakana
milungu Yina***

“...Nadzatilanditsa m'dzanja lanu, mfumu. Koma akapanda kutero, dziwani, mfumu, kuti sitidzatumikira milungu yanu, kapena kulambira fano lagolidi mudalimikalo.”

—Danieli 3:17, 18

WOKANA KRISTU: GONJANI KAPENA MUMVE NJALA

35

Chinakakamiza anthu onse, ang'ono ndi akulu, olemera ndi osauka, mfulu ndi akapolo, kuti alembedwe chizindikiro padzanja lawo lamanja kapena pamphumi pawo. Chinachita zimenezi kuti wina aliyense asalole-dwe kugula kapena kugulitsa kanthu ngati alibe chizindikiro chimenechi. Chizindikiro chake ndicho dzina la chilombo choyamba chija, kapena wêrengo la dzina lake... Yemwe ali ndi nzeru a wêrengere wêrengo la chilombolo, pakuti wêrengolo ndi la munthu. Wêrengo lake ndi 666.

—Chibvumbulutso 13:16-18

Tsiku Labwino Likubwera Kwa Opulumutsidwa

...“Amene wâ ndi amene anali m' masautso akulu aja. Anachapa mikanjo yawo ndi kuiyeretsa m' magazi a Mwanawankhosa. Iwo sadzambvanso njala kapena ludzu. Sadzawambikanso ndi dzu wâ kapena kusauka ndi kutentha. Pakuti Mwanawankhosa uja amene ali pakati pa mpando wachifumu, adzakhala Mbusa wawo, ndipo adzawatsogolera ku akasupe a madzi amoyo. Mulungu adzawapukuta misozi yawo yonse m' maso mwawo.”

—Chibvumbulutso 7:14, 16-17
Kulowa kumwamba ndi njala nkwabwino koposa kulowa ku gehena utakhuta!

ONSE OPEMBEDZA OKANA KRISTU ADZAONONGEDWA, KAPENANSO OKHALA NDI CHIZINDIKIRO PATHUPI PAO KUTI ATHE KUGULA KAPENA KUGULITSA

Kenaka panafikanso mngelo wina wachitatu, wotsatana ndi awiri ena aja. Mokweza mawu iye anati, “Aliyense wopembedza chilombo chija ndiponso fano lake, ndi kulandira chizindikiro chija pamphumi pake kapena padzanja lake, ndiye amene adzamwako vinyo wa ukali wa Mulungu. Vinyoyo adzathiridwa, popanda kanthu kochepetsa mphamvu yake, m’chikho cha mkwiyo wa Mulungu. Munthuyo adzazunzika ndi moto ndiponso ndi miyala yasulufure yoyaka. Zimenezi zidzachiti-

ka pamaso pa angelo a Mulungu, ndiponso pamaso pa Mwanawankhosa uja... Iwo amene anapembedza chilombo chija ndi fano lake, ndiponso amene analandira chizindikiro cha dzina lake chija, sapeza mpumulo usana kapena usiku.” Pambuyo pake ndinamva mawu ochokera Kumwamba. Anati, “Lemba kuti, Ngodala anthu akufa amene kuyambira tsopano afa ali okhulupirira Ambuye.”...

—Chibvumbulutso 14:9-11, 13

CHIGONJETSO CAKUPAMBANA LEMBA NDI FANO LA SATANA USANAFIKE MKWIYO WA MULUNGU PA DZIKO LAPANSI

37

...Panali angelo asanu ndi aŵiri okhala nayo miliri isanu ndi iŵiri. Miliriyo njotsiriza, pakuti ukali wa Mulungu uthera paimeneyi. Kenaka ndinaona ngati nyanja yagalasi losakaniza ndi moto. Ndinaonanso iwo amene anapambana chilombo chija, fano lake lija, ndiponso ŵerengo la dzina lake. Anaimirira pamphepete pa nyanja yagalasi ija, ali ndi azeze amene Mulungu anaŵapatsa. Pambuyo pake ndinamva mawu amphamvu ochokera m'Malo Opatulika muja. Anauza angelo asanu ndi aŵiri aja kuti, "Pitani, katsanuleni padziko lapansi ukali wa Mulungu,

umene uli m'mbale zisanu ndi ziŵiri zija."

—Chibvumbulutso 15:1-2; 16:1

...Ndinaonanso mizimu ya anthu amene anaŵadula pakhosi chifukwa cha kuchitira Yesu umboni, ndiponso chifukwa cha kulalika mawu a Mulungu. Iwo sanapembedze nawo chilombo chija kapena fano lake lija, ndipo anakana kulembedwa chizindikiro chija pamphumi pawo kapena padzanja. Anakhalanso ndi moyo nalamulira pamodzi ndi Kristu zaka sauzande.

—Chibvumbulutso 20:4

HARMAGEDO, NKHONDO YOMWE KRISTU AMALE TSA

Ziwanda Zisonkhanitsira Mafumu Kuti Amenyane Nkhondo

Mizimuyo nja ziwanda, ndipo imachita zozizwitsa. Imapita kwa mafumu a padziko lapansi kukaŵamema, kuti adzabwere kunkhondo ya patsiku lalikulu lija la Mulungu Wamphamvuzonse. Pamenepo mizimu ija inasonhanitsa mafumu aja kumalo amene pa Chiyuda amatchedwa “Harmagedo.”

—Chibvumbulutso 16:14, 16

Kristu Amasula Dziko Lake ndi Anthu Ake Osankhika, Aisrayeli

“Ndipo kudzacitika tsiku ilo, ndidzaika Yerusalemu akhale mwa-

la wolemetsa mitundu yonse ya anthu.... Pamenepo Yehova adzaturuka, nadzacita nkondo ndi amitundu aja, monga anacitira nkondo tsiku lakudumana.” Ndipo mliri umene Yehova adzakantha nao mitundu yonse ya anthu imene idathira nkondo pa Yerusalemu ndi uwu: nyama yao idzaonda akali ciriri pa mapazi ao, ndi maso ao adzapuala m'pfunkha mwao, ndi lilime lao lidzanyala m'kamwa mwao.

—Zekariya 12:3; 14:3, 12

...Popeza kuti Mulungu amatithandiza, kodi angatsutsane nafe ndani?

—Aroma 8:31

KRISTU ADZAPAMBANA KUKHALA MFUMU YOLAMULA DZIKO LONSE LAPANSI

39

M'kamwa mwake munali lupanga lakuthwa lotulukira kunja, loti adza-gonjetsere mitundu ya anthu. Adza-walamulira ndi ndodo yachitsulo, ndipo m'choponderamo mphesa adzaponda mphesa za vinyo wa mkwiyo waukali wa Mulungu Wamphamvuzonse. Pachobvala chake, ndiponso pantchafu yake panalembedwa dzina loti, "Mfumumu ya mafumumu onse, ndi Mbuye wa ambuye onse." —Chibvumbulutso 19:15, 16

"...Ndipo adzalamula mpaka muyaya." —Chibvumbulutso 11:15

***Wokana Kristu Alamulira
Zaka Zochepa. Kristu***

***Alamulira Zaka Zikwi.
Pambuyo Pake Achita Ufumu
Kufikira Nthawi Za Nthawi***

...Koma adzakhala ansembe a Mulungu ndiponso a Yesu Kristu, ndipo adzalamulira pamodzi naye zaka sauzande.

—Chibvumbulutso 20:6

"Ndipo masiku a mafumumu aja Mulungu wa Kumwamba adzaika ufumu woti sudzaonongeka ku nthawizonse...."

—Danieli 2:44

Amitundu onse mudawalenga adzadza nadzagwada pamaso panu, Ambuye; Nadzalemekeza dzina lanu.

—Masalmo 86:9

40 MULUNGU AMAMUPAMBANA NKHONDO SATANA

Chinjoka chachikulu chija china-ponyedwa kunja. Ichochi ndicho njoka yakale ija yotchedwa “Mdyerekezi” ndiponso “Satana”, wonyenga dziko lonse lapansi. Chinaponyedwa padziko lapansi pamodzi ndi angelo ake onse. Pamenepo ndinamva mawu amphamvu Kumwamba alikunena kuti, “Tsopano Mulungu watipulumutsa. Tsopano Mulungu wathu waonetsa mphamvu yake ndiponso ufumu wake. Tsopano Mfumu imene Iye anaidzoza yaonetsa ulamuliro wake. Pakuti woneneza abale athu uja waponyedwa kunja, iye amene ankaŵaneneza kwa Mulungu wathu usana ndi usiku.”

—Chibvumbulutso 12:7-10

Zida Zopambanira Nkhondoyi

“Abale athuwo anamgonjetsa ndi magari a Mwanawankhosa uja, ndiponso ndi mawu a Uthenga umene ankauchitira umboni. Iwo anadzipe-reka kotheratu, kotero kuti sanaope ngakhale kufa.”

—Chibvumbulutso 12:11

Pa Chimaliziro Cha Dziko, Satana Adzaponyedwa Ku Nyanja Yotentha Ndi Moto

Pamenepo Satana amene anaŵanyenga, anaponyedwa m’nyanja yamoto woyaka ndi miyala ya sulufure.... M’menemo adzazunzidwa kwamuyaya usana ndi usiku.

—Chibvumbulutso 20:10

***Kristu Ambuye Alamulira Ku
Nthawi Za Nthawi***

Ukulu, ndi mphamvu, ndi ulemero, ndi kulakika, ndi cifumu ndi zanu, Yehova; pakuti zonse zam'mwamba ndi pa dziko lapansi ndi zanu; ufumu ndi wanu, Yehova; ndipo mwakwezeka mutu wa pa zonse.

—1 Mbiri 29:11

Monga anthu onse amamwalira chifukwa ndi ana a Adamu, mowemonso anthu onse adzauka chifukwa ali mwa Kristu. Koma aliynse adzauka panthaŵi yake: woyambirira ndiye Kristu, ndipo pambuyo pake, pamene Kristuyo adzabwe-ra, iwonso amene ali ake adzauka. Pamenepo chimalizo chidzafika.

Kristu adzathetsa oweruza onse, u-lamuliro wonse, ndi mphamvu zonse, nadzapereka ufumu wonse kwa Mulungu Atate. Pakuti Kristu aye-nera kukhala Mfumu, mpaka Mulungu atagonjetsa adani ake onse. Mdani wotsiriza amene Mulungu adzamthetsa mphamvu, ndiye imfa.

—1 Akorinto 15:22-26

Pambuyo pake mngelo wachisanu ndi chiŵiri analiza lipenga lake, ndipo kunamveka mawu amphamvu Kumwamba. Mawuwo anati, “Tso-pano mphamvu yolamulira dziko la-pansi ili m'manja mwa Ambuyathu ndi mwa Mfumu imene anaidzoza, ndipo adzalamula mpaka muyaya.”

—Chibvumbulutso 11:15

42 SATANA NDI MIZIMU YOIPA NDI ADANI ANU

Satana Amaononga Thupi Ndi Mzimu Pamene Anthu Achita Zoipa Zosiyanasiyana

... Amuna ... akumakhumbana amuna okhaokha. ... anadziitanira chilango chimene chinaŵayenera chifukwa cha ntchito zawo. ...

—Aroma 1:27

Ziripo zinthu ... Mulungu azida; ... manja akupha anthu osacimwa.

—Miyambo 6:16, 17

“Tsono chimapita ndi kukatenga ziŵanda zina zisanu ndi ziŵiri zoiipa koposa ichocho, ndipo chimaloŵa ndi kukhala m’menemo. Choncho mkhalidwe wotsiriza wa munthu uja umaipa koposa mkhalidwe wake woyamba. ...” —Mateo 12:45

Si zododometsa zimenezi ayi, pakuti Satana yemwe amadzizimbaitsa, naoneka ngati mngelo wounikira anthu.

—2 Akorinto 11:14

Funafunani Mulungu Wamoyo Yekha. Osayitana milungu yina yochita zoipa zosiyanasiyana.

Satana, wogalukira Mulungu, amachita zonsezi. Amagwiritsa ntchito anthu, mabukhu, zinthu zowoneka ndi maso, zipembedzo zonama. Zochita zachet poyamba zimaoneka zodabwitsa ndi zothandiza, koma zimapangitsa ukapolo. Kristu yekha angakumasuleni.

Osadzipeleka ku ulamuliro uli wonse womwe si wa Mzimu Woyera Wa Mulungu. Mukhulupilire Bukhu Lopatulika ndi Yesu Kristu.

(Onani Cibvumbulutso 19:13.)

Ciphunzitso chiri chonse chomwe chimakuchotsani ku cikhlukiro, kusambitsidwa, ndi chiombolo kupyolera mu mwazi wa Kristu ndi chonyenga.

Yesu anaŵayankha kuti, “Chenje-rani kuti wina aliyense asadzakunyengeni. Chifukwa kudzafika anthu ambiri m’dzina langa nadzane-na kuti, ‘Mpulumutsi wolonjezedwa uja ndine’, ndipo adzasokeretsa anthu ambiri. Kudzaoneka aneneri onama ambiri, amene azidzasokeretsa anthu ambiri.”

—Mateo 24:4, 5, 11

Ndakhala ndilikukuuzani kaŵirikaŵiri, ndipo tsopano ndilikubwe-

rezanso kukuuzani molira misozi, kuti alipo ambiri amene mayende-dwe awo amatsimikizira kuti ndiwo adani a mtanda wa Kristu. Potsiriza adzawonongeka. Mimba yawo ndiyo mulungu wawo....

—Afilipi 3:18, 19

Mwazi Wopambana Wa Kristu Umawombola

... Sanakuwomboleni ndi ndalama zimene zimawonongeka, koma anakuwombolani ndi imfa yamtengo wapatali ya Kristu, amene anakhala ngati mwanawankhosa wopanda banga kapena chilema. Mwa iye mukhulupirira Mulungu....

—1 Petro 1:18, 19, 21

***Wolamulidwa Ndi Chikhalidwe
Cha Uchimo***

Pakuti ife tonse takhala ngati wina amene ali wosakonzeka; ndi zolungama zathu zonse ziri ngati cobvala codetsedwa.... —Yesaya 64:6

***Mkwiyo Pa Mzimu Wa
Kusamvera***

Panthaŵi imeneyo, mayendedwe anu analikulingana ndi mayendedwe a anthu ongokonda zapansi pano, ndipo munalikumvera mkulu wa aulamuliro mumlengalenga. Mkuluyo ndi mzimu woipa umene ulikugwira ntchito tsopano pakati pa anthu osamvera Mulungu. Nthaŵi ija tonsefe tinalinso ndi moyo wonga wawo, ndipo tinalikutsata zilakolako za

khalidwe lathu lokonda zoipa. Tinkachitanso zilizonse zimene matupi athu ndi maganizo athu analikufuna.... —Aefeso 2:2, 3

***Satana Ndiye mbuye Wa
Osapulumsidwa***

Koma ngati Uthenga Wabwino umene timalalika uli wophimbikabe, ngophimbika kwa okhawo amene alikutayika. Iwoŵa sakhulupirira, popeza kuti Satana, amene ali mulungu wa dziko lino lapansi, anachititsa khungu maganizo awo, kuopa kuti angaone kuŵala kwa Uthenga Wabwino. Kuŵalako kumaonetsa ulemmerero wa Kristu, ndipo mwa Iyeyu Mulungu mwini amaoneka. —2 Akorinto 4:3, 4

“Munda uja ndiwo dziko lapansi. Mbewu zabwino zija ndiwo anthu amene ali a Ufumu wa Mulungu. Namsongole uja ndiwo anthu a Wo-
ipa uja.”
—Mateo 13:38

“Inu ndinu ana a Satana. Iye ndiye tate wanu, ndipo mulikufuna kumachita zimene tate wanuyo amalalaka...”
—Yohane 8:44

Mwa Adamu, Ndife Ogalukira Mulungu

“Munthu amene sabvomerezana ndi Ine, amatsutsana nane. Ndipo amene sasonkhanitsa pamodzi ndi Ine, ameneyo amamwaza.”
—Mateo 12:30

Ichi Ndi Chifukwa Chake

Tiyenera Kubadwanso Mwa Mzimu

Ngati munthu ali mwa Kristu, ngolengedwa kwatsopano. Zakale zapita, ndipo zimene zilipo nza-tsopano.
—2 Akorinto 5:17

Dzipelekeni Kwa Ambuye Yesu Kristu Tsopano

...Mvetsani, yino ndiyo nthawi yabwino imene Mulungu alikukomera anthu mtima. Lero ndilo tsiku la chipulumutso. —2 Akorinto 6:2

Koma tikamabvomera machimo athu, Mulungu amene ali wokhulupirika ndi wolungama, adzatichululukira machimo athuwo. Adzatichululukira ndi kutichotsera kusalungama kwathu konse. —1 Yohane 1:9

Tsono ndani angatilekanitse ndi chikondi cha Kristu? Masautso kodi, kapena zoŵaŵa, kapena mazunzo, kapena njala, kapena usiŵa, kapena zoopsa, kapenanso kuphedwa? Koma pazonsezi tili opambana ndithu chifukwa cha Iye amene anatikonda. —Aroma 8:35, 37

Chifukwa aliyense amene ali mwana wa Mulungu, amagonjetsa dziko lapansi. Chimene timagonjetsera nacho dziko lapansilo, ndicho chikhulupiriro chathu. —1 Yohane 5:4

Amapeleka Mphotho Kwa Onse Opambana

“Amene ali nawo makutu, amve zi-

mene Mzimu Woyera alikuuza mipingo. Amene adzapambane, ndidzampatsa chakudya cha Kumwamba, chosaoneka ndi maso. Ndidzampatsanso mwala woyera wolembedwapo dzina latsopano, lodziŵa iye yekha, osati wina aliyense.”

—Chibvumbulutso 2:17

“Amene adzapambane ndi kuchita mpaka potsiriza zimene ndamlamula, ndidzampatsa ulamuliro pamitundu yonse ya anthu.”

—Chibvumbulutso 2:26

Muli wofunika kwa Mulungu. Chifukwa cha Kalvari. Mulungu ali wofunika kwa inu!

MUDZISANKHIRE AMENE MUDZAMTUMIKIRA NTHAWI YOSATHA

47

Kuoneka Ndi Kristu Mu Ulemelero

Munaukitsidwa pamodzi ndi Kristu, tsono ikani mtima pazinthu za Kumwamba, kumene Kristu alikhala kudzanja lamanja la Mulungu. Muzifunafuna za Kumwamba, osati za pansi pano. Kristu ndiye moyo wanu, ndipo pamene Iye adzaonekere, inunso mudzaonekera muulemerero pamodzi naye. Chifukwa cha zinthu zotere Mulungu amakwiwira anthu osamumvera.

—Akolose 3:1, 2, 4, 6

Kapena Kutembereredwa Ndi Satana Kwamuyaya

“Pamenepo idzauzanso a kudzanja

lake lamanzere aja kuti, ‘Chokani, inu anthu otembereredwa. Pitani kumoto wosatha umene Mulungu anakonzera Satana ndi angelo ake.’”

—Mateo 25:41

Oipawo adzabwerera kumanda, Inde amitundu onse akuiwala Mulungu.

—Masalmo 9:17

“Ndipo ngati dzanja lako likuchimwitsa, lidule. Ndi bwino koposa kuti ukaloŵe kumoyo wosatha uli woduka dzanja, kupambana kuti ukaloŵe uli ndi manja onse aŵiri ku Gehena, kumoto wosazimika.”

—Marko 9:43

Mudzichepetse Nokha

Apo Yesu anaitana mwana namuimiritisa pakati pawo, ndi kuwauza kuti, “Zoonadi ndikukuuzani kuti mukapanda kusinthika ndi kukhala ngati ana, simudzaloŵa konse mu Ufumu wa Kumwamba. Nchifukwa chake munthu amene adzichepetsa ngati mwana uyu, ameneyo ndiye wamkulu mu Ufumu wa Kumwamba.”

—Mateo 18:2-4

Lapani Machimo

Zimenezi zinachitikadi pamene Yohane Mbatizi anafika kuchipululu, nayamba kulalika. Ankauza anthu kuti, “Lapani, batizidwani, ndipo Mulungu adzakhululukira

machimo anu.” Yohane uja ataponyedwa m’ndende, Yesu anapita ku Galilea alikulalika Uthenga Wabwino wochokera kwa Mulungu. Ankati, “Nthaŵi yakwana, Mulungu ali pafupi kukhazikitsa ufumu wake tsopano. Lapani ndi kukhulupirira Uthenga Wabwinowu.”

—Marko 1:4, 14, 15

“Iyayi, koma ngati simulapa, inunso mudzawonongedwa monga iwo aja.”

—Luka 13:3

“Nchifukwa chake lapani, bwere-rani kwa Mulungu, kuti akufafanizireni machimo anu.” —Ntchito 3:19

(Mau akupitilira pa tsamba linalo.)

LANDIRANI KRISTU MONGA MPULUMUTSI WANU LERO!

Mudzipereke Nokha Kwa Yesu Kristu

Pereka njira yako kwa Yehova;
khulupiriranso Iye, adzacicita.

–Masalmo 37:5

“Pakuti Mulungu anakonda anthu a padziko lonse lapansi kwambiri. Anali naye Mwana mmodzi yekha, komabe anampereka kuti aliyense wokhulupirira Iyeyo asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.”

–Yohane 3:16

...“Khulupirira Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka iwe ndi a m’banja mwako.” –Ntchito 16:31

Komabe anthu onse amene anamlandira ndi kumkhulupirira, Iye anaapatsa mphamvu yokhala ana a Mulungu. –Yohane 1:12

Bvomerezani Kristu Poyera

...Ubvomereza pakamwa pako kuti Yesu ndiye Ambuye, ndipo ngati ukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka. Chifukwa munthu ayenera kukhulupirira ndi mtima wake, kuti Mulungu amlungamitse, ndipo ayenera kubvomereza chikhulupiriro chakecho pakamwa pake, kuti apulumuke. –Aroma 10:9-10

Scripture text reprinted from the Bible in Chichewa by permission of United Bible Societies Africa Regional Centre, Nairobi, Kenya.

Published in numerous languages by World Missionary Press, Inc., as God supplies funds in answer to prayer. **For questions or more information by country, visit: www.wmp-contacts.org**

World Missionary Press
PO Box 120
New Paris, IN 46553-0120 USA
www.wmpress.org

3-23



Read booklets online or by App
www.wmp-readonline.org
1440 Chichewa SVC